# Malongosoledwe a coonadi ca m'Baibulo

## Za imfa ya Yesu ndi kuuka kwake

1. Yesu anatifera
2. Yesu akhalanso ndi moyo
3. Yesu anadzionetsa kwa anzake

# 1. Yesu anatifera

*Nditaya moyo wanga cifukwa ca nkhosa – Yohane 10.15*

**Kuwerenga**
Yohane 19.11-18

**Malongosoledwe**
Kodi mudziwa maina a masiku onse a pa sabata? Tsiku la Sabata, Lolemba, Laciwiri, Lacitatu, Lacinai, Lacisanu ndi Loweruza.
Kuli tsiku Lacisanu limodzi lochedwa Lacisanu Labwino kapena Lacisanu Loyera kapena Good Friday. Caka ciriconse timakumbukira Lacisanu Labwino tisanakumbukire kuuka kwa Yesu pa tsiku la Pasaka.
Cinthu cacisoni cacikulu cinacitika pa Tsiku Lacisanu Labwino. Yesu anafa pa Lacisanu Labwino. Anafa pa mtanda. Paliponse pomwe Yesu anapita Iye anacita zabwino nthawi zonse. Koma anthu ena anamuda. Kodi mukumbukira mdani wamkulu wa Mulungu? Inde, Satana ndi mdani wa Mulungu. Satana azonda Mulungu. Ndipo ayesa kupangitsa anthu kukhalanso ozonda Mulungu. Pamene Yesu anali pa dziko lapansi, Satana anayesadi kupangitsa anthu kukhala akuzonda Yesu.
Tsiku lina iwo amene anada Yesu, anampereka kwa Pilato wolamulira. Iwo anati kwa Pilato, 'Yesu uyu ndi Munthu woipa. Abvuta. Angakhale afuna kukhala mfumu. Tiyenera kumcotsa.'
Pilato ananena, 'Kodi Iye anacita zoipa zotani?'
Kunalibe munthu womwe anganene cinthu coipa cimodzi cocitidwa ndi Yesu. Koma ananena, 'Iye ayeneradi kufa. Muyenera kumpacika!'
Pilato anamva manthu cifukwa ca anthu awa. Anadziwa kuti Yesu anali Munthu wabwino. Koma analola anthu kutenga Yesu. Anati, 'Mtengeni kumpacika'.
Ndipo iwo anacita tero.
Anatenga Yesu ku phiri lochedwa Golgota. Anamkhoma pa mtanda. Ndipo anaika mtanda pa dothi.
Yesu anakhala pa mtanda kungakhale kunali dzuwa lotentha. Misomali yokhala m'manja ndi mapazi ake inawawa. Patapita kanthawi Iye anafa.
Tingawerenge izi zonse m'Baibulo. Nthano iyi ndi nthano ya Lacisanu Labwino.
Kodi tsiku Lacisanu ilo lacisoni linalidi tsiku labwino?
Inde, Lacisanu ilo linali Lacisanu labwino loposa. Linali tsiku labwino cifukwa Yesu anatifera. Anafa kuti macimo athu acotsedwe, kuti tipite Kumwamba ndi kukhala naye muyayaya.
Mulungu Atate anatuma Yesu kutifera. Ndipo Yesu anataya moyo wake cifukwa ca ife.

**Kukambirana**
1. Ndi ciani cimene cinacitika pa tsiku Lacisanu Labwino?
2. Ndi cifukwa ciani tsiku ilo ndi tsiku labwino?
3. Cikhululukiro ca macimo athu ndi cotheka cifukwa ca Yesu yekha. Baibulo likamba m'2 Akorinto 5.21, 'Ameneyo sanadziwa ucimo anamyesera ucimo m'malo mwathu; kuti ife tikhale cilungamo ca Mulungu mwa Iye'. Fotokozani citanthauzo ca ndime iyi:
    a. Kodi ndi yani amene sanadziwe ucimo?
    b. Nanga ife anthu timadziwa uchimo?
    c. Kutanthauzanji kuti Yesu anafa m'malo mwa ocimwa kodi?
    d. Kukhala mwa Yesu kutanthauzanji kodi?
    e. Kodi macimo anu anakhululukidwa ndi Yesu?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Yesu Kristu, Sitikwaniritsa kukulemekezani moyenerera. Tikuyamikani kuti munafa pa mtanda. Munafera anthu ocimwa, olephera ndi osowa. Cikondi canu ndi cacikulu! Tiribe ciyembekezo ciriconse koma Inu nokha. Mutikonze kuti tilingana ndi Inu. Tikupemphani izi m'dzina lanu, Amen.

## 2. Yesu akhalanso ndi moyo

*Anaukitsidwa tsiku lacitatu, monga mwa malembo – 1 Akorinto 15.4b*

**Kuwerenga**
Mateyu 28.1-8

**Malongosoledwe**
Ophunzira a Yesu anamva cisoni kwambiri pamene Yesu anafa. Iye anali Bwenzi lao lapamtima. Adayembekezera Iye kukhala Mpulumutsi wao. Koma adafa. Kodi Yesu angakhale bwanji Mpulumutsi wao ngati anali wakufa? Iwo sanamvetse.
Anaika Yesu m'manda: manda osemedwa m'mwala. Anakunkhunizira mwala waukulu pa khomo la manda. Kenaka anapita ku nyumba.
Adani a Yesu anati, 'Tidzaika alonda pa manda, cifukwa ophunzira a Yesu angabwere kuba mtembo wa Yesu. Atacita tero anganene kuti Yesu akhalanso ndi moyo!'
Koma ophunzira a Yesu sanaganizire za kuba mtembo wa Yesu kapena za kunena kuti Iye akhalanso ndi moyo. Anadziwa kuti Yesu adafadi ndipo anamva cisoni cacikulu.
Alonda anakhala pa manda usiku, usana wonse pa tsiku Laciweru ndiponso usiku uyo. Sanakonde kukhala pa manda usiku wonse. Analakalaka kutuluka kwa dzuwa. Ndiye pa tsiku la Sabata pamene dzuwa linayamba kutuluka, iwo anakhala okondwera.
Koma, mwadzidzidzi, ndi ciani ico? Kunali kuunika monga mphenzi. Inacokera kumwamba koma siinali mphenzi yeniyeni. Alonda anaiona: inali mngelo wotsikira Kumwamba! Anaona kuti mngelo anapita ku mwala pa khomo pa manda. Anaona kuti iye anakunkhunzira mwala. Ndipo mngelo anakhala pamwamba pace! Alonda anamva mantha kwambiri kotero kuti anagwa nkhope zao pansi. Sanayerekezebe kuona. Patapita kanthawi anaimirira nathamanga. Anathamanga mofulumira kucokera ku manda.
Kenaka munakhala bata m'munda. Dzuwa linatuluka. Azimai ena anakwera pa phiri laling'ono. Iwo anali anzake a Yesu. Anadza kubweretsa zonunkhira kuziika m'manda.
Anadabwa pamene anaona kuti mwala wacotsedwa. Anati, 'Ndi yani amene adakhala pano nacotsa mwala kodi? Ndi ciani cimene cidacitika?'
Anafulumira kukaona m'manda. M'menemo anaona mngelo. Anamva mantha.
Angelo anati kwa iwo, 'Musaope. Muli kufuna Yesu. Iye mulibe muno iai. Anauka! Bwerani kuona kuti mulibe muno'.
Azimai anapita m'manda naona kuti Yesu munalibe. Anathamanga kukauza ophunzira uthenga wabwino: 'Yesu anauka!'
Petro ndi Yohane anathamanga ku manda mofulumira. Sanaone mngelo. Koma anaona kuti Yesu munalibe m'manda. Anazindikira kuti Yesu adauka. Yesu akhala ndi moyo! Iye ndiye Mpulumutsi ndithu!
Inde, Yesu anafa. Koma anauka kwa akufa kukhala ndi moyo muyayaya. Iye ndiye Kristu, Mwana wa Mulungu. Mngelo anakunkhunzira mwala kuti anthu onse angaone kuti Yesu sanali m'manda. Anauka kwa akufa kuonetsa kuti ndiye Mwana wa Mulungu.

**Kukambirana**
1. Ndi ciani cimene cinacitika pamene mngelo anatsika Kumwamba?
2. Ndi cifukwa ciani mngelo anakunkhunzira mwala?
3. Ndi yani amene anamva mantha kodi?
4. Nanga ndani anakondwera?
5. Yesu akhala wamoyo. Apatsa moyo wosatha kwa iwo onse olapa ndi kudalira pa Iye pa cipulumutso cake. Kodi mwalandira moyo wosatha?

**Citsanzo ca pemphero:**
Ambuye Yesu, Tikuyamikani kuti mukhala ndi moyo. Ndinu Mpulumutsi wodabwitsa. Mutipatse umoyo wa uzimu. M'dzina lanu tikupemphani izi, Amen.

## 3. Yesu anadzionetsa kwa anzake

*Ndi Wamoyoyo; ndipo ndinali wakufa, ndipo taona, ndiri wamoyo kufikira nthawi za nthawi – Cibvumbulutso 1.18a*

**Kuwerenga**
Yohane 21.1-8

**Malongosoledwe**
Kunali usiku. Tsiku la kuuka kwa Yesu kunapita. Azimai adauza ophunzira a Yesu za manda wopanda Yesu, za mngelo ndiponso kuti mngelo anati kuti Yesu akhala ndi moyo. Petro ndi Yohane adatamanga kukaona manda wopanda mtembo wa Yesu. Koma iwo sadaone mngelo.
Ophunzira a Yesu anasonkhana m'cipinda cimodzi. Anakhoma citseko, cifukwa anamva mantha. Anaganiza kuti adani atapha Yesu angabwere kuwatenganso ukapolo.
Mwadzidzidzi Petro analowamo. Anaoneka wosangalala kwambiri. Anati, 'Ndaona Yesu. Alankhula ndi ine!'
Ophunzira ena anapukusa mitu. Analephera kukhulupirira kuti Yesu anacoka m'manda ndipo kuti akhala ndi moyo ndithu. 'Si cotheka', iwo anayankha.
'Odi! Odi!' Kunali munthu pa citseko. Munthu wina anati, 'Tiloleni kulowamo! Tiri ndi uthenga wabwino!' Munthuyo anali Kleopa. Ophunzira anamdziwa. Kleopa anali mnzao wabwino. Ophunzira anatsegula citseko. Kleopa analowa pamodzi ndi mwamuna wina. Ndipo anaoneka okondwa kwambiri.
Pamene munthu wina anali kukhomanso citseko, Kleopa anati, 'Taona Yesu! Ayenda nafe ndi kulankhula nafe. Atiuza cifukwa cake ca imfa yake!'
Ophunzira anati, 'Petro aonanso Yesu! Koma ndi cotheka bwanji kuti Yesu akhalanso ndi moyo?'
Ndipo pa nthawi imeneyo Yesu yemwe anali m'cipindaco mosayembekezera. Anakhalamo, anawayang'ana ndi cikondi ndipo ananena, 'Mtendere ukhale ndi inu!'.
Ophunzira a Yesu anadabwa. Kodi Iye ndiye Yesu ndithu? Yesu anawaonetsa manja ndi mapazi ake m'mene misomali idalimo. Ndipo anawaonetsa nthithi yake m'mene msirikali adambaya. Koma ophunzira analepherabe kukhulupirira. Koma pamene Yesu anadya nsomba ndi uci iwo anadziwa kuti Munthuyo ndi Yesu ndithu. Iye anali Ambuye ao okondedwa womwe akhalanso ndi moyo.
Kenaka Yesu anawauza cifukwa cake ca imfa yake. Kalekale Mulungu adalonjeza kutuma Mpulumutsi. Yesu anauza ophunzira ake kuti Iye yemwe ndiye Mpulumutsi. Mulungu adamtuma kufa cifukwa ca macimo a dziko lapansi ndiponso kuti apulumutsa anthu ake kuti iwo akhale naye muyayaya.
Yesu sanali cikhalire ndi ophunzira ake. Anacokapo ndipo ophunzira ake sanamuone kanthawi. Koma Yesu anabweranso. Masiku makhumi anai anadzionetsa kawirikawiri. Anafuna kuti ophunzira atsimikize kuti Iye akhaladi ndi moyo.
Tsiku lina Yesu anawakumana nao pa nyanja ya Galileya ndipo anadya pamodzi cakudya ca m'mawa.
Tsiku lina Yesu anadza ku anzake mazana asanu. Anawaonekera pa nthawi imodzi. Oo, iwo anakondwera kwambiri pamene anaona Yesu!

**Kukambirana**
1. Kodi Yesu anaonekera bwanji ophunzira ake?
2. Kodi ophunzira a Yesu anadziwa bwanji kuti Munthuyo ndi Yesu yemwe?
3. Kodi tidziwa bwanji kuti Yesu akhala ndi moyo?
4. 1 Akorinto 15.17: 'Ndipo ngati Kristu sanaukitsidwa, cikhulupiriro canu ciri copanda pace; muli cikhalire m'macimo anu'. Ndi cifukwa ciani kuuka kwa Yesu ndi kofunikira kwambiri kulingana ndi ndime iyi?
5. Kodi kuukitsidwa kwa Yesu kutanthauza ciani kwa inu?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Yesu, sitikhoza kukuonani. Koma tidziwa kuti mukhala ndi moyo. Inu ndinu Mpulumutsi wamoyo. Mutidalitse ndi kukhululukira macimo athu onse. Mutiphunzitse kucita zabwino. Tikupemphani izi m'dzina lanu. Amen.

Zolembedwa zina za m'bukuli zinasandulidwa kucokera mu buku la 'Schoolland, Marian. M. (1962), *Leading Little Ones To God* (21st ed), Wm. B. Eerdmans Publishing Company.'
© Stephanos Zambia Trust